# Initial Primary Teacher Education

## Buku lophunzitsira
## m'sukulu za uphunzitsi

# Chichewa

## Buku 4

Malawi Institute of Education

# Initial Primary Teacher Education

## Buku lophunzitsira
## m’sukulu za uphunzitsi

# Chichewa

## Buku 4

**Malawi Institute of Education**

**Omwe adalemba ndi kusindikiza bukuli**
Malawi Institute of Education
P O Box 50
Domasi
Malawi

Email: miedirector@sdnp.org.mw
Website: www.mie.edu.mw

© Malawi Institute of Education 2018

Zonse za m'bukumu n'zosati munthu akopere mu njira ina iliyonse popanda chilolezo. N'zosatinso munthu achitire malonda mpang'ono pomwe. Komabe ngati munthu afuna kugwira ntchito ya za maphunziro ndi bukuli, ayambe wapempha ndi kulandira chilolezo kuchokera kwa eni ake omwe adalisindikiza.

# Mawu otsogolera

Maphunziro ndi maziko a chitukuko m'dziko. Iwo ndi gwero la chitukuko pa moyo wa munthu, gulu la anthu ngakhalenso dziko. Maphunziro amakonzekeretsa ophunzira kukhala ndi maluso oti azithandiza kutukula moyo wa anthu ndi chuma cha dziko moyenera. Makolo amafuna kuti ana awo azikula ndi nzeru zabwino komanso moyo wathanzi kudzera m'maphunziro omwe angawathandize kukhala ndi maluso ndi maganizo abwino kuti akhale anthu odalirika ndi okondwa.

Choncho n'koyenera kuti maphunziro azikhala othandiza ophunzira kukhala a makhalidwe abwino, maganizidwe oyenera komanso odziwa udindo wawo. Ophunzira uphunzitsi aziphunzitsidwa moyenera kuti azitha kuphunzitsa mwaluso.

Pali zinthu zambiri zimene zimathandiza kuti maphunziro akhale apamwamba. Chimodzi mwa izo ndi kukhala ndi aphunzitsi osulidwa bwino. Aphunzitsi ali ndi gawo lalikulu pamaphunziro chifukwa ndiwo amatsogolera ophunzira kupeza nzeru za maphunziro. Iwo amakhalanso chitsanzo kwa ophunzira m'machitidwe awo.

Cholinga cha maphunziro a zauphunzitsi m'Malawi ndi kusula aphunzitsi ogwira ntchito yawo mwaluso ndi mwaukadaulo. Izi zimatheka ngati aphunzitsiwo aphunzitsidwa mwaluntha kuti akhale ndi nzeru, maluso ndi ukadaulo wowathandiza kuphunzitsa ophunzira akupulayimale moyenera. Choncho maphunziro a uphunzitsi a IPTE aunikidwanso ndi cholinga choti ophunzira uphunzitsi akamatsiriza maphunziro awo azikhala atasulidwa bwino kuti akagwire ntchito yawo mwaukadaulo.

Ndondomeko younikanso maphunzirowa yatsogoleredwa ndi lingaliro ili:

'Kusula mphunzitsi wotha kudziunika, wodzidalira, wozindikira kuti kuphunzira sikutha pa moyo wa munthu, wamakhalidwe abwino komanso wodziwa kuphunzitsa ophunzira osiyanasiyana molingana ndi kuthekera kwawo.'

Tikukhulupirira kuti aphunzitsi ndi ophunzira m'sukulu zophunzitsa ntchito yauphunzitsi m'Malawi muno azindikira kuti maphunzirowa ndi aphindu pothandiza ophunzira uphunzitsi kukhala ndi maziko odalirika pa ntchito yawo.

Dr William Susuwele-Banda
Executive Director
**Malawi Institute of Education**

## Kuthokoza

Unduna wa za Maphunziro, Sayansi ndi Luso pamodzi ndi Malawi Institute of Education ukuthokoza anthu onse amene adathandiza mu njira zosiyanasiyana kuti bukuli lilembedwe.

Akuthokoza makamaka bungwe la UNICEF ndi GIZ chifukwa cha thandizo la chuma ndi upangiri osiyanasiyana pa nthawi yolemba bukuli.

Undunawu ukuthokozanso mwapadera Mkulu wa Department of Inspectorate and Advisory Services (DIAS), a Raphael Agabu, ndi onse ogwira ntchito ku Dipatimentiyi, Mkulu wa Malawi Institute of Education, Dr William Susuwele-Banda, ndi onse ogwira ntchito kumeneko, Mtsogoleri wa ntchito yokonzanso maphunziro a m'sukulu za uphunzitsi (IPTE), a Edward Gobede-Mtonga ndi onse owathandizira (a Loyce Chisale, Anthony Malunga ndi Catrin Anderer) chifukwa chotsogolera ntchito yolemba bukuli.

MIE ndi Undunawu akuthokozanso a Frackson Manyamba, Foster NJ Gama, Benjamin David, Margaret Magalasi ndi Victor Mwakanema pounika bukuli ndi kupereka malangizo othandiza.

**Okonza**

**Mkonzi** : Max J Iphani
**Wotayipa ndi kuyala bukuli** : Catherine Katete
**Mkonzi wamkulu** : Max J Iphani

## Olemba

| | | |
|---|---|---|
| Innocencia Guzako-Kachala | - | Lilongwe Teachers' College |
| John Kunkumbira | - | St Joseph's Teachers College |
| Gertrude Mkandawire | - | Blantyre Teachers' College |
| Laston Mkhaya | - | Montfort Special Needs College (Rtd) |
| Ndamyo Mwanyongo | - | Kasungu Teachers' College |
| Wisdom Nkhoma | - | Domasi College of Education |

# Zamkatimu


| | | |
|---|---|---|
| Mawu otsogolera | …………………………………………………………. | v |
| Kuthokoza | ……………………………………………………………..… | vi |
| Mutu 1 | Kuphunzitsa ndi kuyesa ndakatulo ndi nyimbo ………………..… | 1 |
| Mutu 2 | Kuphunzitsa malonje ……………..………..……………………….. | 4 |
| Mutu 3 | Kuphunzitsa ndi kuyesa kuwerenga ………………………………. | 8 |
| Mutu 4 | Kuphunzitsa kulemba chimangirizo ndi kalata mu Sitandade 4 mpaka 8…………………….……………………….... | 12 |
| Mutu 5 | Kuphunzitsa kulemba lembetso ndi zidziwitso mu Sitandade 3 mpaka 8……………..……………..………………………….. | 15 |
| Mutu 6 | Kuphunzitsa akapandamneni …………………………………... | 18 |
| Mutu 7 | Kuphunzitsa mitundu ya ziganizo………………………………… | 21 |
| Mutu 8 | Kuphunzitsa nthambi za chiganizo …………………………………… | 24 |
| Mutu 9 | Kuphunzitsa ndi kuyesa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani/nthano, macheza ndi sewero …………………………..... | 28 |
| Mutu 10 | Kuphunzitsa nsinjiro zachiyankhulo ……………………….………. | 32 |
| Mutu 11 | Kuphunzitsa mtantho wa mawu ………………………………………… | 36 |

# MUTU 1 Kuphunzitsa ndi kuyesa ndakatulo ndi nyimbo

**Luso** Kumva ndi kuyankhula
**Nthawi** Maola 5
**Chigawo** Chachitatu

## Chiyambi

Ndakatulo ndi nyimbo ndi zina mwa zinthu zomwe zimakometsa chiyankhulo. Pali zifukwa zambiri zophunzitsira ndakatulo ndi nyimbo m'sukulu za pulayimale.

M'mutu uno muunika momwe munkaphunzitsira ndakatulo ndi nyimbo. Mukumbutsana zifukwa zophunzitsira ndakatulo ndi nyimbo kwa ophunzira akupulayimale. Muunikanso ndondomeko yoyenera kutsatira pophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza ndondomeko yomwe ankatsatira pophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo.
- apeka ndakatulo ndi nyimbo.
- alakatula ndakatulo/aimba nyimbo.

## Mawu otsogolera

Kuphunzitsa ndakatulo ndi nyimbo n'kofunika kwambiri. Ndakatulo ndi nyimbo zimathandiza ophunzira kufotokoza zomwe zili m'maganizo awo kudzera mu kulatula kapena kuimba. Zimathandizanso kusunga chikhalidwe cha makolo komanso kupereka maphunziro osiyanasiyana. Izi zingathandizenso ophunzira kukhala ndi luso la ntchito yomwe angadzagwire m'tsogolo monga kulemba, kulakatula ndakatulo komanso kuimba nyimbo.

Aphunzitsi ayenera kukhala ndi luso lophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo kuti azitha kuphunzitsa mwaukadaulo.

### Ntchito 2 Kufotokoza ndondomeko yophunzitsira ndakatulo ndi nyimbo

Kutsatira ndondomeko pophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo n'kofunika chifukwa ophunzira amamvetsa bwino zoyenera kuchita. Tsopano muunika ndondomeko yomwe munkatsatira pophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo.

**Zochita 1 Kukambirana kufunika kophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo**

1 Kambiranani matanthauzo a mawu otsatirawa: ndakatulo, kulakatula ndi nyimbo.
2 Fotokozani kufunika kophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo kwa ophunzira a m'sukulu za pulayimale.
3 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kuunika ndondomeko yomwe munkatsatira pophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo**

1 Fotokozani ndondomeko yomwe munkatsatira pophunzitsa ndakatulo ndi nyimbo.

2 Kambiranani mavuto omwe munkakumana nawo pogwiritsa ntchito ndondomeko imeneyi.
3 Perekani njira zomwe mungagwiritse ntchito pofuna kuthetsa mavuto omwe munkakumana nawo.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

## Ntchito 2 Kupeka ndakatulo ndi nyimbo

Tsopano muphunzira kupeka ndakatulo ndi nyimbo. Kudziwa kupeka ndakatulo ndi nyimbo kukuthandizani kukaphunzitsa ophunzira anu mosavuta.




### Zochita 1 Kuzukuta ndakatulo ndi nyimbo

1 Kambiranani mfundo zoyenera kutsatira popeka ndakatulo ndi nyimbo.
2 Zukutani ndakatulo ndi nyimbo zomwe aphunzitsi anu akupatsani potsatira mfundo zomwe mwakambirana.
3 Perekani maganizo anu pa ndakatulo ndi nyimbo zomwe mwazukuta.

### Zochita 2 Kulemba ndakatulo ndi nyimbo

1 Kambiranani mfundo zoyenera kutsatira popeka ndakatulo ndi nyimbo.
2 Lembani ndakatulo kapena nyimbo m'magulu mwanu.
3 Werengerani anzanu ndakatulo kapena nyimbo zomwe mwalemba.
4 Zukutani ndakatulo ndi nyimbo zomwe mwamvetsera.

## Ntchito 3 Kulakatula ndakatulo ndi kuimba nyimbo

M'gawo lino, mulakatula ndi kuimba nyimbo zomwe mwalemba. Kenaka musonyeza momwe mungaphunzitsire ndi kuyesa ndakatulo ndi nyimbozi.

### Zochita 1 Kulakatula ndakatulo ndi kuimba nyimbo

1 Kambiranani momwe mungalakatulire ndakatulo ndi kuimba nyimbo zomwe mwalemba.
2 Konzekerani momwe mungalakatulire ndakatulo komanso mungaimbire nyimbo zanuzo kwa anzanu onse.
3 Lakatulani ndakatulo ndi kuimba nyimbo zanu.
4 Perekani ndemanga pa ndakatulo ndi nyimbo zomwe mwamvetsera.
5 Fotokozani phunziro lomwe likupezeka mu ndakatulo ndi nyimbo zomwe mwamvetsera.

**Zochita 2 Kuphunzitsa kulakatula ndakatulo ndi kuimba nyimbo**

1. Kambiranani momwe mungaphunzitsire kulakatula ndakatulo ndi kuimba nyimbo.
2. Phunzitsani ndakatulo ndi nyimbo zomwe munapeka.
3. Perekani maganizo anu pa momwe maphunziro ayendera.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

1. Mukonzeretu ndondomeko yophunzitsira ndakatulo ndi nyimbo.
2. Muonetsetse kuti ophunzira akupeka ndakatulo/nyimbo potsatira ndondomeko yoyenera.
3. Muotsetsenso kuti ophunzira akulakatula mopatsa chidwi potsatira izi:
   - kukweza ndi kutsitsa kwa mawu koyenera.
   - kutchula mawu motsindika.
   - Kulakatula mwanthetemya kapena kuimba nyimbo mwa mingoli.
   - kusonyeza kukondwa kapena chisoni.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaunika momwe munkaphunzitsira ndakatulo ndi nyimbo. Mwafotokoza zifukwa zosiyanasiyana zophunzitsira ndakatulo komanso nyimbo kwa ophunzira a m'sukulu za pulayimale. Mwaphunziranso kupeka ndi kulakatulo ndakatulo komanso kuimba nyimbo mwaluso kuti zipereke matanthauzo oyenera kwa omvera. Pomaliza, mwapereka ndondomeko yoyenera kutsatira pophunzitsa kulakatula ndakatulo ndi kuimba nyimbo.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1. Perekani zifukwa zophunzitsira ndakatulo ndi nyimbo.
2. Fotokozani ndondomeko yophunzitsira ndakatulo ndi nyimbo m'sukulu za pulayimale.
3. Kodi mlakatuli ayenera kukhala ndi maluso ati kuti ndakatulo yake ipereke tanthauzo loyenera?

## Matanthauzo a mawu

**Ndakatulo:** Maganizo olembedwa mwachidule m'ndime kapena Mwampululira

**Kulakatula:** Kunena za muntima

**Nyimbo:** Maganizo amene amanenedwa kudzera m'kuimba.

## Mabuku


Malawi Institute of Education, (2008). *Maphunziro a m'sukulu zauphunzitsi Chichewa Buku la mphunzitsi.* Domasi: Malawi Institute of Education.

Malawi Institute of Education, (2008). *Maphunziro a m'sukulu zauphunzitsi Chichewa Buku la ophunzira.* Domasi: Malawi Institute of Education.


## Kuwerenga koonjezera


Ministry of Education, Science and Technology, (2009). *Initial primary teacher education through open and distance learning. Module 2.* Lilongwe: Department of Teacher Education and Development (DTED).

# MUTU 2 Kuphunzitsa malonje

| | |
|---|---|
| **Luso** | Kumva ndi kuyankhula |
| **Nthawi** | Maola 4 |
| **Chigawo** | Chachitatu |

## Chiyambi

M'mutu uno, mukumbutsana mitu yosiyanasiyana ya kumva ndi kuyankhula m'makalasi onse a m'sukulu za ku pulayimale. Ina mwa mitu ya kumva ndi kuyankhula ndi malonje, zouzidwa ndi maliwu. Mufotokoza malo osiyanasiyana kumene anthu amalonjerana pa moyo wawo wa tsiku ndi tsiku. Pomaliza, muphunzitsa kapena kuonerera phunziro la malonje ndi cholinga choti mupeze njira zothetsera mavuto omwe mudakumana nawo pamene munkaphunzitsa malonje pa maluso a kumva ndi kuyankhula.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza mitu yosiyanasiyana yophunzitsira kumva ndi kuyankhula m'makalasi onse akupulayimale.
- afotokoza komwe anthu amalonjerana.
- asonyeza momwe adaphunzitsira malonje apauzimba, apamatenda, apamsonkhano komanso akunyumba.

## Mawu otsogolera

Maluso a kumva ndi kuyankhula ndi maluso awiri osiyana. Ngakhale malusowa ali awiri choncho, mphunzitsi ayenera kuphunzitsa malusowa nthawi imodzi popeza kumva ndi kuyankhula kumachitika nthawi imodzinso. Pali ntchito zosiyanasiyana zophunzitsira malusowa monga malonje, malangizo ndi mauthenga. Panthawi yomwe munkaphunzitsa malusowa mudakumana ndi zovuta zambiri monga kuchuluka kwa ophunzira komanso kusowa kwa zipangizo zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera.

Kudziwa kaphunzitsidwe koyenera ka malusowa kumathandiza mphunzitsi kuphunzitsa mwaukadaulo ndi mwachikoka. Ophunzira nawonso amaphunzira kagwiritsidwe ntchito koyenera ka chiyankhulo pa zochitika zosiyanasiyana. M'mutu uno, muunika momwe munkaphunzitsira malonje. Kuonjezera apo, muphunzitsa mutu wa malonje kuti mupeze ndi kukonza zolakwika zomwe mudakumana nazo pamene munkaphunzitsa malonje osiyanasiyana m'sukulu zomwe munkaphunzitsa.

### Ntchito 1 Kufotokoza za mitu ya kumva ndi kuyankhula

M'mbuyomu, mudaphunzira mitu yosiyanasiyana yophunzitsira maluso a kumva ndi kuyankhula. M'gawo lino, muunika momwe mudaphunzitsira malusowa.

**Zochita 1 Kuunika mitu yophunzitsira maluso a kumva ndi kuyankhula**

1 Fotokozani mitu yophunzitsira maluso a kumva ndi kuyankhula yomwe ikupezeka m′silabasi ndi mabuku ophunzitsira m′sukulu za pulayimale.
2 Kambiranani njira zomwe mungagwiritse ntchito pophunzitsa mitu yosiyanasiyana ya kumva ndi kuyankhula yomwe mwatchula.
3 Unikani momwe ntchito yophunzitsa kumva ndi kuyankhula idayendera m′sukulu zomwe munkaphunzitsa
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kukambirana mavuto omwe mudakumana nawo**

1 Kambiranani mavuto omwe mudakumana nawo pophunzitsa maluso a kumva ndi kuyankhula.
2 Fufuzani njira zomwe mungagwiritse ntchito kuti muthetse mavuto omwe mwatchula.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

## Ntchito 2 Kukambirana za malo osiyanasiyana kumene anthu amalonjerana

Anthu amalonjerana pa malo osiyanasiyana molingana ndi zochitika za pamalopo. M′gawo lino, mukambirana za malo osiyanasiyana kumene anthu amalonjerana ndi nthawi yake.




**Zochita 1 Kufotokoza za malo amene anthu amalonjerana ndi nthawi yake**

1 Pezani malo osiyanasiyana kumene anthu amalonjerana ndi nthawi yake pogwiritsa ntchito mabuku ophunzitsira ndi ophunzirira Chichewa m′sukulu zapulayimale.
2 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Zochita 2 Kukambirana kufunika kopereka malonje molingana ndi malo komanso nthawi**

Kambiranani nkhani yotsatirayi:
Bambo Salambula adali mkulu wa mpingo. Tsiku lina kudachitika maliro. Bambo Salambula adapatsidwa udindo wotsogolera mwambo wa malirowo. Iwo adati, "Moni mabwana ndi madoma. Ife tonse tabwera pano chifukwa chauta watigwera. Choncho tili ndi chisoni chambiri. Tsopano tifuna tiyambe mwambo wa maliro."
Tsopano yankhani mafunso otsatirawa:

1 Kodi ndi mtundu wanji wa malonje womwe waperekedwa mu nkhaniyi?
2 Kambiranani zomwe zalakwika m′malonjewa.

3 Fotokozani momwe bambo Salambula akadaperekera malonjewa moyenera.
4 N'chifukwa chiyani ophunzira ayenera kuphunzira kupereka malonje moyenera?

### Ntchito 3 Kuphunzitsa malonje

Mwaunika mavuto osiyanasiyana omwe mudakumana nawo pophunzitsa malonje. Mwafufuzanso njira zothandizira kuthetsa mavuto omwe mudakumana nawo. M'gawo lino, muphunzitsa malonje osiyanasiyana.

**Zochita 1 Kukambirana ndondomeko yophunzitsira malonje**

1 Kambiranani ndondomeko yomwe mudagwiritsa ntchito pophunzitsa malonje osiyanasiyana.
2 Konzani phunziro losonyeza momwe mungaphunzitsire malonje osiyanasiyana.
3 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kusonyeza kuphunzitsa malonje**

1 Kambiranani momwe mungaphunzitsire malonje osiyanasiyana.
2 Sonyezani momwe mungaphunzitsire malonjewo.
3 Zukutani maphunzirowo.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Muonetsetse kuti ophunzira ali ndi zipangizo zoyenera kukonzekera phunziro la malonje.
- Mukonzeretu ndondomeko yophunzitsira malonje osiyanasiyana.
- Muombe mkota pa mitundu ya malonje ndi kaphunzitsidwe kake.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaunika momwe mungaphunzitsire ntchito zomwe zingakulitse maluso a kumva ndi kuyankhula. Mwafotokoza mitu yosiyanasiyana ya kumva ndi kuyankhula komanso malo omwe anthu amalonjerana. Mwafotokozanso momwe munkaphunzitsira malonje osiyanasiyana ndipo mwaphunzitsa ndi kuona maphunziro a malonje. Pomaliza, mwakambirana njira zothetsera mavuto amene mudakumana nawo pophunzitsa malonje m'sukulu zomwe munkaphunzitsa. Zina mwa njira zomwe mwapeza ndi kugwiritsa ntchito njira zophunzitsira, zophunzirira ndi zoyesera zoyenera komanso kukonzeratu zipangizo zoyenera.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Tchulani njira zitatu zomwe mungagwiritse ntchito pophunzitsa malonje mu Sitandade 1.
2 Fotokozani momwe mungaphunzitsire malonje apamalonda mu Sitandade 4.

3 Kodi kufunika kwa gawo losonyeza ophunzira zoyenera kuchita m'ndondomeko ya phunziro la malonje n'kotani?

## Mabuku

Malawi Institute of Education, (2008). *IPTE Chichewa buku la ophunzira*. Domasi: Malawi Institute of Education.

Malawi Institute of Education, (2008). *Maphunziro a m'sukulu zauphunzitsi m'Malawi: Chichewa buku la mphunzitsi*. Domasi: Malawi Institute of Education.

Ministry of Education, Science and Technology, (2010). *Initial primary education through open and distance learning Chichewa: Module 1*. Lilongwe: Department of Teacher Education and Development.

# MUTU 3 Kuphunzitsa ndi kuyesa kuwerenga

| | |
|---|---|
| **Luso** | Kuwerenga |
| **Nthawi** | Maola 4 |
| **Chigawo** | Chachitatu |

## Chiyambi

M'mbuyomu, mudaphunzira momwe mungaphunzitsire kuwerenga ndipo mudaphunzitsa kuwerenga m'sukulu zapulayimale.

M'mutu uno, mufotokoza zomwe mudakumana nazo pophunzitsa kuwerenga. Mufotokozanso njira zomwe mudagwiritsa ntchito pophunzitsa kuwerengako. Kenaka, musonyeza kagwiritsidwe ntchito ka njirazo.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza njira zomwe adagwiritsa ntchito pophunzitsa kuwerenga.
- aphunzitsa ndi kuyesa kuwerenga.

## Mawu otsogolera

Ophunzira a m'sukulu zapulayimale amawerenga mokweza ndi mwachinunu. Pali njira zosiyanasiyana zophunzitsira kuwerenga mokweza monga kuwerenga kwa mavume, kwa m'magulu komanso kwa mmodzimmodzi. Pamene ophunzira akuwerenga pogwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana, mphunzitsi ayenera kuwayesa. Mphunzitsi angayese kawerengedwe ka ophunzira pogwiritsa ntchito njira izi:

1 Kugwiritsa ntchito chipangizo chotchedwa 'running record'. Kuyesa ophunzira pogwiritsa ntchito chipangizochi, mphunzitsi amayesa momwe wophunzira aliyense akutchulira mawu, njira zomwe akugwiritsa ntchito powerenga, nthawi yomwe wawerenga komanso ngati akumvetsa zomwe akuwerengazo. Kenaka, mphunzitsi amawerengera momwe wophunzirayo wakhozera pa kawerengedwe kake pa ndime yomwe anapatsidwa. Pomaliza, mphunzitsi amadziwa mabuku oyenera kumupatsa wophunzirayo kuti apititse patsogolo luso lake la kuwerenga.

2 Kugwiritsa ntchito chipangizo choonerera komanso kulemba momwe ophunzira akuwerengera (*Observation checklist*). Pogwiritsa ntchito chipangizochi mphunzitsi amakonza mafunso omwe agwiritse ntchito poyesa kawerengedwe ka wophunzira aliyense. Onani chitsanzo chotsatirachi:

| **Kodi wophunzira** | **Akukhoza kwambiri** | **Akukhoza bwino** | **Akukhoza pang'ono** | **Ndi wofunika chithandizo** |
|---|---|---|---|---|
| 1 akutchula mawu moyenera?<br>2 akuwerenga mosadodoma?<br>3 akuwerenga mofulumira?<br>4 akumvetsa zomwe akuwerenga? | | | | |

Pogwiritsa ntchito chipangizochi, aphunzitsi amalembamo mfundo zosiyanasiyana zomwe akufuna kuyesa ophunzira.

3 Kugwiritsa ntchito chipangizo chotchedwa 'Fluency rubric' (Muyeso wa kawerengedwe). Chipangizochi ndi chomwe mphunzitsi amagwiritsa ntchito polemba muyeso wa kawerengedwe ka ophunzira. Mwachitsanzo:

Muyeso wa kawerengedwe (*Fluency rubric*)

| | | |
|---|---|---|
| wophunzira wofunika chithandizo | 1 | akuwerenga mawu amodzi amodzi kapenanso akulephera kuwerenga. |
| wophunzira wokhoza pang'ono | 2 | akuyesera kuwerenga magulu a mawu koma sakumvetsa zomwe akuwerenga. |
| wophunzira wokhoza bwino | 3 | akuyesera kuwerenga mofulumira ndi momveka bwino. |
| wophunzira wokhoza kwambiri | 4 | akuwerenga bwino kwambiri, akumvetsa zomwe akuwerenga ndipo akugwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana powerenga. |

Kuyesa ophunzira kumathandiza mphunzitsi pamodzi ndi ophunzira kudziwa momwe akuwerengera ndi mavuto omwe akukumana nawo powerenga. Izi zimathandizanso mphunzitsi kupeza njira zoyenera kuthandizira ophunzirawo.

## Ntchito 1 Kufotokoza njira zomwe munkagwiritsa ntchito pophunzitsa kuwerenga

Kumbukirani zomwe munkachita pophunzitsa kuwerenga. Maphunziro ena adakusangalatsani pomwe ena adali ndi zovuta zina. Tsopano muunika zomwe mudakumana nazo pophunzitsa komanso mavuto omwe mudawapeza.

### Zochita 1 Kufokotokoza zomwe mudakumana nazo pophunzitsa kuwerenga




1 Tengani mafayilo anu ndipo muwerenge zotsatira za ntchito yomwe ndaphunzitsa.
2 Kambiranani zomwe mudakumana nazo kuchokera pa zomwe mwawerenga m'mafayilo anu zokhudza kuphunzitsa kuwerenga.
3 Perekani maganizo anu pa zomwe mwawerenga.

### Zochita 2 Kuunika mavuto omwe mudakumana nawo pophunzitsa kuwerenga

1 Kambiranani mavuto omwe mudakumana nawo pophunzitsa kuwerenga.
2 Fotokozani njira zomwe mungagwiritse ntchito kuti muthetse mavuto omwe munkakumana nawo.
3 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

## Ntchito 2 Kuphunzitsa kuwerenga

Kuphunzitsa ndi kuyesa ophunzira moyenera pamene akuphunzira kuwerenga n'kofunika. Tsopano muphunzitsa kuwerenga komanso muunika njira zoyesera zomwe mungagwiritse ntchito pophunzitsa kuwerenga.

### Zochita 1 Kuphunzitsa luso la kuwerenga

1 Kambiranani momwe mungaphunzitsire kuwerenga pogwiritsa ntchito njira zomwe mwakambirana.
2 Phunzitsani kuwerenga pogwiritsa ntchito njira zomwe mwakambirana.
3 Zukutani maphunzirowo.

### Zochita 2 Kuyesa ophunzira luso la kuwerenga

1 Unikani njira zomwe munkagwiritsa ntchito poyesa ophunzira pa luso la kuwerenga.
2 Kambiranani mavuto omwe munkakumana nawo pogwiritsa ntchito njira zomwe mwatchula.
3 Fotokozani njira zomwe mungagwiritse ntchito kuti muthetse mavutowo.
4 Sonyezani anzanu momwe mungagwiritsire ntchito njirazo.
5 Perekani maganizo anu pa ntchito yomwe anzanu achita.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.
- Mukhaliretu ndi njira zoyesera ophunzira pa luso la kuwerenga.
- Mulimbikitse ophunzira kusonyeza kagwiritsidwe ntchito ka njira zophunzitsira ndi kuyesera kuwerenga.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwafotokoza njira zomwe munkagwiritsa ntchito pophunzitsa komanso kuyesa ophunzira pa luso la kuwerenga. Mwafotokozanso njira zomwe mungagwiritse ntchito pothetsa mavuto omwe mungakumane nawo pophunzitsa luso la kuwerenga. Pomaliza, mwaphunzitsa kuwerenga pogwiritsa ntchito njira zophunzitsira komanso zoyesera lusoli.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Tchulani njira zosiyanasiyana zomwe zimathandiza kuthetsa mavuto omwe aphunzitsi amakumana nawo pophunzitsa kuwerenga.
2 Fotokozani njira zomwe mungagwiritse ntchito pophunzitsa ndi kuyesa luso la kuwerenga.
3 Mphunzitsi wina pasukulu yanu amakonda kugwiritsa ntchito njira ya mavume nthawi zonse pophunzitsa kuwerenga. Ndi malangizo otani omwe mungapereke kwa mphunzitsiyu.

## Mabuku


Cunningham, PM & Allington, RL, (2011). *Classrooms that work: they can all read and write*. Fifth Edition. Boston: Pearson.

Malawi Institute of Education, (2008). *Chichewa buku la mphunzitsi.* Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education, (2008). *English tutor's handbook.* Domasi: MIE.

# MUTU 4 Kuphunzitsa kulemba chimangirizo ndi kalata mu Sitandade 4 mpaka 8

**Luso** Kulemba
**Nthawi** Maola 4
**Chigawo** Chachitatu

## Chiyambi

M'chigawo choyamba mudaphunzira kalembedwe ka chimangirizo ndi kalata zomwe zimathandiza ophunzira kukulitsa luso la kulemba. Chimangirizo komanso kalata zimayenera zilembedwe mu dongosolo loyenera kuti owerenga athe kumvetsa uthenga womwe walembedwa.

M'mutu uno, mufotokoza momwe munkaphunzitsira chimangirizo ndi kalata m'sukulu zomwe munkaphunzitsa. Musonyezanso kaphunzitsidwe koyenera ka chimangirizo ndi kalata.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza momwe ankaphunzitsira chimangirizo ndi kalata m'sukulu zomwe ankaphunzitsa.
- aphunzitsa anzawo kalembedwe koyenera ka chimangirizo ndi kalata.

## Mawu otsogolera

Kulemba chimangirizo ndi kalata kumafuna kuganizira zinthu zambiri. Zina mwa zinthuzi ndi kusankha mutu womwe wophunzira sangavutike kupeza mfundo zikuluzikulu, kusagwiritsa ntchito mawu olaula kapena achipongwe komanso kulemba malembo ooneka bwino. Kuonjezera apo, polemba chimangirizo ndi kalata pamafunika kulemba chikonzero chomwe chimathandiza mlembi kusanja mfundo mu ndondomeko yoyenera kuchokera pa mutu womwe wasankha.

Mphunzitsi akadziwa kulemba chimangirizo ndi kalata moyenera angathe kuthandiza ophunzira kulemba ntchito zimenezi mosavuta. Pa chifukwa ichi, mutu uno ukuthandizani kudziwa zofunika kutsatira pophunzitsa kulemba chimangirizo ndi kalata.

### Ntchito 1 Kufotokoza momwe munkaphunzitsira kulemba chimangirizo ndi kalata m'sitandade 4 mpaka 8

Tsopano mukambirana zomwe mudakumana nazo nthawi yomwe munkaphunzitsa m'sukulu zapulayimale. Mufotokozanso mavuto omwe mudakumana nawo ndi njira zomwe zingathandize kuthetsa mavutowo.

**Zochita 1 Kuunika zomwe mudakumana nazo pophunzitsa kulemba chimangirizo ndi kalata**

1 Kambiranani momwe munkaphunzitsira kalembedwe ka

chimangirizo ndi kalata mu sukulu za pulayimale zomwe munkaphunzitsa.
2 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kupeza njira zothetsera mavuto omwe mudakumana nawo pophunzitsa chimangirizo ndi kalata**




1 Fotokozani mavuto omwe mudakumana nawo pophunzitsa chimangirizo ndi kalata.
2 Perekani njira zomwe mungagwiritse ntchito pofuna kuthetsa mavuto omwe munkakumana nawo.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

## Ntchito 2 Kuphunzitsa kalembedwe ka chimangirizo ndi kalata m'sitandade 4 mpaka 8

M'gawo lino, muphunzitsa kulemba chimangirizo ndi kalata m'makalasi osiyanasiyana. Poyamba mufufuza m'mabuku a ophunzira ntchito zokhudza chimangirizo ndi kalata. Kenaka, muphunzitsa kulemba chimangirizo ndi kalata.

**Zochita 1 Kufufuza ntchito zokhudza chimangirizo ndi kalata m'mabuku a ophunzira**

1 Pezani ntchito zokhudza chimangirizo ndi kalata m'mabuku a ophunzira.
2 Kambiranani zomwe mwapeza m'makalasi a 1 mpaka 4 ndi 5 mpaka 8.
3 Perekani maganizo anu pa zomwe mwapeza.

**Zochita 2 Kuphunzitsa kulemba chimangirizo ndi kalata**

1 Unikani ndondomeko yomwe munkatsatira pophunzitsa kulemba chimangirizo ndi kalata.
2 Kambiranani ndondomeko yoyenera kutsatira pophunzitsa kalembedwe ka chimangirizo ndi kalata.
3 Konzani ndondomeko yophunzitsira kalembedwe ka chimangirizo ndi kalata m'magulu mwanu.
4 Phunzitsani chimangirizo ndi kalata.
5 Zukutani momwe phunziro layendera.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mulimbikitse ophunzira kufufuza njira zothandizira kuthetsa mavuto omwe ankawalepheretsa kuphunzitsa chimangirizo ndi kalata moyenera.
- Muombe mkota pa ndondomeko yoyenera yophunzitsira kalembedwe ka chimangirizo ndi kalata.

## Kufotokoza mwachidule

Pophunzitsa chimangirizo ndi kalata ndi kofunika kuti ophunzira adziwe bwino njira ndi ndondmeko zoyenera kutsatira.

M'mutu uno, mwafotokoza mavuto omwe munkakumana nawo pophunzitsa kalembedwe ka chimangirizo ndi kalata kwa ophunzira m'sukulu zapulayimale zomwe munkaphunzitsa. Mwafotokozanso mavuto amene mudakumana nawo pophunzitsa ndi njira zomwe mungagwirirtse ntchito pofuna kuthetsa mavutowo. Pomaliza, mwaphunzitsa chimangirizo ndi kalata potsatira ndondomeko yoyenera.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani zomwe mwachita bwino komanso zomwe mwalephera pa mutu uno.
2 Ophunzira anu akulephera kulemba chimangirizo ndi kalata moyenera. Fotokozani zomwe mungachite kuti muwathandize ophunzirawa kulemba chimangirizo ndi kalata moyenera komanso mopatsa chidwi.
3 N'chifukwa chiyani mphunzitsi ayenera kutsatira ndondomeko yoyenera pophunzitsa kalembedwe ka chimangirizo ndi kalata?

## Mabuku

Malawi Institute of Education, (2008). *Buku la mphunzitsi*. Domasi: Malawi Institute of Education.

Ngoma, SJL & Chauma, AM, (2014). *Tizame m'Chichew: malamulo ophunzitsira ndi kuphunzirira Chichew*a. Blantyre: Bookland International.

## Kuwerenga koonjezera

Nkhoma, WA, (1999). *Kuphunzitsa Chinyanja*. Zomba: Chancellor College Publications.

# MUTU 5 Kuphunzitsa kulemba lembetso ndi zidziwitso mu Sitandade 3 mpaka 8

**Luso** Kulemba
**Nthawi** Maola 3
**Chigawo** Chachitatu

## Chiyambi

M'mbuyomu, mudaphunzira kuphunzitsa ndi kuyesa kulemba lembetso ndi zidziwitso. Mudaphunziranso momwe zinthu ziwirizi zimathandizira ophunzira kukulitsa luso lawo la kulemba.

M'mutu uno, muunikanso ndondomeko yomwe ingatsatidwe pophunzitsa kulemba lembetso ndi zidziwitso ndi cholinga choti mukaphunzitse ophunzira moyenera.

## Zizindikiro zakakhozedwe

Pakutha pa mutu uno ophunzira:

- afotokoza momwe adaphunzitsira kalembedwe ka lembetso m'sukulu zomwe ankaphunzitsa.
- aphunzitsa lembetso potsatira ndondmeko yoyenera.

## Mawu otsogolera

Kuphunzitsa kulemba lembetso ndi zidziwitso ndi zina mwa ntchito zofunika kwambiri pophunzitsa luso la kulemba. Kulemba lembetso ndi zidziwitso kumathandiza ophunzira kulemba mawu ndi ziganizo pa mtima, kulemba zizindikiro zam'kalembedwe, kukulitsa luso la kumva ndi kuyankhula, kulemba mwachangu komanso molondola, ndi kukhazikitsa maziko antchito yodzagwira m'tsogolo monga ulembi ndi ukonzi. Mwapadera, kulemba lembetso kumathandizanso ophunzira kumvetsera mwatcheru zomwe wina akukamba kapena kuwerenga ndi kuwerenga zomwe iwo kapena wina walemba.

Pali mavuto osiyanasiyana omwe aphunzitsi amakumana nawo pophunzitsa kulemba lembetso ndi zidziwitso. Ena mwa mavutowa ndi kusatsatira ndondomeko yoyenera ndi kusagwiritsa ntchito zipangizo pophunzitsa. Monga aphunzitsi muyenera kuphunzira kaphunzitsidwe koyenera ka lembetso ndi zidziwitso. Izi zikuthandizani kupeza njira zoyenera kugwiritsa ntchito pophunzitsa kuti ophunzira apindule.

### Ntchito 1 Kufotokoza momwe munkaphunzitsira kalembedwe ka lembetso ndi zidziwitso

Tsopano muunika momwe munkaphunzitsira kulemba lembetso ndi zidziwitso. Kuunikaku n'kofunika kwambiri chifukwa kukuthandizani kukonza zomwe simumazidziwa bwino.

**Zochita 1 Kuunika momwe munkaphunzitsira lembetso ndi zidziwitso**

1 Kambiranani momwe munkaphunzitsira kalembedwe ka lembetso ndi zidziwitso m'sukulu zosiyanasiyana zomwe munkaphunzitsa.
2 Fotokozani mavuto omwe munkakumana nawo pophunzitsa lembetso ndi zidziwitso.
3 Kambiranani njira zomwe mungagwiritse ntchito pofuna kuthetsa mavutowo.
4 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kuunika ndondomeko yomwe munkagwiritsa ntchito pophunzitsa kalembedwe ka lembetso ndi zidziwitso**

1 Unikani ndondomeko yomwe munkatsatira pophunzitsa lembetso ndi zidziwitso.
2 Fotokozani mavuto omwe mudakumana nawo pogwiritsa ntchito ndondomeko yomwe mwatchula.
3 Perekani njira zomwe mungagwiritse ntchito pofuna kuthetsa mavuto omwe munkakumana nawo.

## Ntchito 2 Kuphunzitsa lembetso ndi zidziwitso potsatira ndondomeko yoyenera

Tsopano muonerera aphunzitsi anu akuphunzitsa kulemba lembetso ndi zidziwitso. Kenaka, inunso muphunzitsa potsatira momwe aphunzitsi anu achitira. Kuonerera momwe ena amaphunzitsira ntchito zosiyanasiyana n'kofunika kwambiri chifukwa kumathandiza kuphunzira maluso omwe ena alinawo.

**Zochita 1 Kuonerera phunziro la lembetso ndi zidziwitso**

1 Kambiranani momwe mungaphunzitsire lembetso ndi zidziwitso potsatira njira zomwe mwakambirana.
2 Konzani ndondomeko yophunzitsira kalembedwe ka lembetso ndi zidziwitso mu Sitandade 3 mpaka 8.
3 Onererani phunziro la lembetso pamene aphunzitsi anu akuphunzitsa.
4 Perekani ndemanga pa momwe phunzirolo layendera.

**Zochita 2 Kuphunzitsa kalembedwe ka lembetso ndi zidziwitso**

1 Konzekerani kuphunzitsa phunziro la lembetso ndi zidziwitso.
2 Sonyezani anzanu kaphunzitsidwe koyenera ka lembetso ndi zidziwitso.
3 Zukutani phunziro lomwe mwaphunzitsa.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mulimbikitse ophunzira kufufuza njira zothandizira kuthetsa mavuto omwe adakumana nawo pophunzitsa lembetso ndi zidziwitso.
- Mukonzeretu ndondomeko yophunzitsira lembetso ndi zidziwitso.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwafotokoza zomwe munkachita pophunzitsa lembetso ndi zidziwitso. Mwaunika mavuto omwe mudakumana nawo pophunzitsa komanso mwafotokoza njira zomwe mungagwiritse ntchito pophunzitsa kalembedwe ka lembetso ndi zidziwitso pofuna kuthetsa mavutowo. Mwaunikanso ndondomeko yoyenera kutsatira pophunzitsa lembetso ndi zidziwitso. Kenaka, mwaonerera kaphunzitsidwe koyenera ka lembetso. Pomaliza, mwaphunzitsa lembetso ndi zidziwitso.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani njira zomwe zingamuthandize mphunzitsi kuphunzitsa lembetso ndi zidziwitso moyenera.
2 N'chifukwa chiyani mphunzitsi ayenera kuphunzitsa lembetso mu Sitandade 3 mpaka 8?
3 Mwapeza kuti aphunzitsi a Sitandade 1 ndi 2 pa sukulu yanu sakuphunzitsa zidziwitso. Ndi malangizo otani omwe mungapereke kwa aphunzitsi otere?

## Mabuku

Malawi Institute of Education, (2008). *Buku la mphunzitsi m'makoleji a mphunzitsi*. Domasi: Malawi Institute of Education.

Ngoma, SJL & Chauma, AM, (2014). *Tizame m'Chichewa: malamulo ophunzitsira ndi kuphunzirira Chichew*a. Blantyre: Bookland International.

## Kuwerenga koonjezera

Nkhoma, WA, (1999). *Kuphunzitsa Chinyanja*. Zomba: Chancellor College.

# MUTU 6 Kuphunzitsa akapandamneni

**Luso** Kugwiritsa ntchito malamulo achiyankhulo
**Nthawi** Maola 3
**Chigawo** Chachitatu

## Chiyambi

M'mbuyomu, mudaphunzira mitundu ya mawu yosiyanasiyana monga dzina, mlowam'malo, mfotokozi ndi muonjezi. M'malamulo achiyankhulo mumapezekanso magulu a mawu. Limodzi mwa maguluwa ndi kapandamneni.

M'mutu uno, muphunzira mitundu ya akapandamneni. Musonyeza momwe mungaphunzitsire mitundu yosiyanasiyana ya akapandamneniwa.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza mitundu ya akapandamneni.
- aphunzitsa akapandamneni.

## Mawu otsogolera

Kapandamneni ndi gulu la mawu m'chiganizo lomwe limakhala lopanda mneni. Gululi silipereka ganizo lomveka bwino popeza lilibe mneni. Akapandamneni alipo osiyanasiyana molingana ndi ntchito zawo. N'kofunika kuti aphunzitsi muzisiyanitsa akapandamneni ndi magulu ena a mawu monga nthambi za chiganizo zosaima pazokha kuti muziphunzitsa ophunzira molondola. Kudziwa bwino kuphunzitsa akapandamneni kungathandize ophunzira kuzindikira gulu la mawu limeneli mosavuta. Motero, mutu uno ukuthandizani kuzindikira mitundu ya akapandamneni ndi momwe mungaphunzitsire.

### Ntchito 1 Kufotokoza mitundu ya akapandamneni

Cholinga cha ntchito ino ndi choti muzindikire za akapandamneni ndi mitundu yawo. Izi zikuthandizani kukonzekera kuphunzitsa moyenera.

**Zochita 1 Kufotokoza tanthauzo la akapandamneni**

1 Kambiranani tanthauzo la kapandamneni lomwe laperekedwa m'mawu otsogolera a mutu uno.
2 Pezani akapandamneni m'ziganizo zomwe mwapatsidwa.
3 Uzani anzanu zomwe mwapeza.

**Zochita 2 Kufufuza mitundu ya akapandamneni**

1 Kambiranani mitundu yosiyanasiyana ya akapandamneni.
2 Pezani akapandamneni a mitundu yosiyanasiyana yomwe mwakambirana.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

### Ntchito 2 Kuphunzitsa mitundu ya akapandamneni

Tsopano musonyeza momwe mungaphunzitsire akapandamneni. Kenaka, mufotokoza momwe

mungagwiritsire ntchito njira ya K-W-L pophunzitsa ntchitoyi.




**Zochita 1 Kuphunzitsa mitundu ya akapandamneni**

1 Konzekerani kuphunzitsa mtundu wa kapandamneni womwe mwapatsidwa.
2 Sonyezani momwe mungaphunzitsire mtundu wa kapandamneniyo.
3 Zukutani maphunzirowo.

**Zochita 2 Kufotokoza njira ya K-W-L pophunzitsa mitundu ya akapandamneni**

1 Mphunzitsi mnzanu pasukulu yanu wakuuzani kuti akufuna kuphunzitsa akapandamneni pogwiritsa ntchito njira ya K-W-L m'gawo loyamba la phunziro lake koma njirayi sakuidziwa kwenikweni. Kambiranani mfundo zomwe angatsate.
2 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.
3 Perekani maganizo anu pa ubwino wotsatira njirayi.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mupezeretu zitsanzo zokwanira za mitundu ya akapandamneni yosachepera isanu ndi umodzi (6).
- Muombe mkota pa zomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira za akapandamneni. Mwaphunzira tanthauzo la kapandamneni ndi mitundu yake. Pomaliza, mwaphunzitsa mitundu yosiyanasiyana ya akapandamneni ndipo mwazukuta maphunzirowo.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Perekani mitundu ya akapandamneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:
   a. Usamayende m'mbali mwa msewu.
   b. Iye wagula malaya okongola kwabasi.
   c. Ndamanga nyumba yaikulu ndithu.
   d. Kuledzera ndi kuphwanya malamulo asukulu.
   e. Anthuwo ankayenda mofulumira kwambiri.
2 Kodi mungaphunzitse bwanji ophunzira kuti amvetse mosavuta mitundu ya akapandamneni?

## Mabuku

Ngoma, SJL ndi Chauma, AM, (2014). *Tizame m'Chichewa: malamulo ophunzitsira ndi kuphunzirira Chichew*a. Bookland International, Blantyre.

Nkhoma, WA, (1999). *Kuphunzitsa Chinyanja*. Zomba: Chancellor College.

# MUTU 7 Kuphunzitsa mitundu ya ziganizo

| | |
|---|---|
| **Luso** | Kugwiritsa ntchito malamulo achiyankhulo |
| **Nthawi** | Maola 4 |
| **Chigawo** | Chachitatu |

## Chiyambi

M'mbuyomu, mudaphunzitsa ophunzira anzanu malamulo a chiyankhulo pa mitu yomwe munasankha. Ndi bwino kuti mupitirize kuyesera kuphunzitsa ndi cholinga choti mupititse patsogolo nzeru zanu komanso ukadaulo wa uphunzitsi.

M'mutu uno, muphunzira mitundu ya ziganizo ndipo muphunzitsa mitunduyo.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza mitundu ya ziganizo.
- aphunzitsa mitundu ya ziganizo.

## Mawu otsogolera

Chiganizo ndi gulu la mawu lokhala ndi mneni lomwe limapereka ganizo lomveka bwino. Pali mitundu yaikulu inayi ya ziganizo. Mitunduyo ili motere: chiganizo chopanda nthambi, chiganizo cha ziganizo zingapo, chiganizo chanthambi ndi chiganizo cha ziganizo zanthambi.

Ophunzira akadziwa bwino mitundu ya ziganizo, adzagwiritsa ntchito chiyankhulo moyenera popanga ziganizo zomveka bwino pamene akufotokoza kapena kulemba nkhani.

Pophunzitsa mitundu ya ziganizo mphunzitsi ayenera kusankha njira yogwiritsa ntchito. Pali njira yotsogolera, njira yosatsogolera ndi njira yakasakaniza. Chotero mukuyenera kudziwa bwino mitundu ya ziganizo ndi njira zomwe mungaphunzitsire kuti ophunzira akamvetse mitunduyi ndi kuigwiritsa ntchito moyenera.

### Ntchito 1 Kufotokoza mitundu ya ziganizo

Tsopano mukambirana za mitundu ya chiganizo komanso mupeza ntchito zokhudza mitundu ya ziganizo m'mabuku a ophunzira a Sitandade 5 mpaka 8.

**Zochita 1 Kukambirana mitundu ya ziganizo**

1 Kambiranani tanthauzo ndi zitsanzo za mitundu inayi ya ziganizo: chiganizo chopanda nthambi, chiganizo cha ziganizo zingapo, chiganizo chanthambi ndi chiganizo cha ziganizo zanthambi.
2 Lembani zomwe mwapeza.
3 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kufufuza mitundu ya ziganizo m'mabuku a Sitandade 5 mpaka 8**

1 Fufuzani ntchito zokhudza mitundu ya ziganizo m'mabuku a ophunzira.
2 Kambiranani zomwe mwapeza.

3 Perekani maganizo anu pa ntchitoyi.

**Ntchito 2 Kuphunzitsa mitundu ya ziganizo**

M'gawo lino, musonyeza kuphunzitsa mitundu ya ziganizo komanso mukonza ntchito yomwe ophunzira anu angakachitire kunyumba.




**Zochita 1 Kuphunzitsa mitundu ya ziganizo**

1 Konzekerani kuphunzitsa mtundu wa chiganizo womwe mwapatsidwa.
2 Phunzitsani phunziroli.
3 Kumbukirani kuyesa ophunzira pamene mukuphunzitsa.
4 Unikani momwe phunziro lililonse layendera.

**Zochita 2 Kukonza ntchito yokachitira kunyumba**

1 Sankhani mtundu umodzi wa ziganizo.
2 Konzani ntchito yoti ophunzira anu akachitire kunyumba. Mulemberetu mayankho a ntchitoyo.
3 Zukutani ntchito zomwe mwakonza ndipo konzani zomwe sizinalembedwe bwino.
4 Uzani anzanu kufunika kopatsa ophunzira ntchito yokachitira kunyumba.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Musankhe ophunzira ena kuti aphunzitse maphunziro a mitundu ya ziganizo potsatira njira yotsogolera, yosatsogolera kapena yakasakaniza.
- Muombe mkota pa zomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira mitundu inayi ya ziganizo ndi zitsanzo zake. Mitunduyi ndi chiganizo chopanda nthambi, chiganizo cha ziganizo zingapo, chiganizo chanthambi ndi chiganizo cha ziganizo zanthambi. Pomaliza, mwaphunzitsa ndi kuzukuta phunziro la mitundu ya ziganizo.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Kodi mwaphunzira zinthu ziti pamene mumaphunzira mitundu ya ziganizo?
2 Fotokozani kusiyana pakati pa 'chiganizo chanthambi' ndi 'chiganizo cha ziganizo za nthambi'.
3 Pa njira zosiyanasiyana zophunzitsira malamulo achiyankhulo, ndi njira iti yomwe yakusangalatsani pa phunziro la mitundu ya ziganizo? Fotokozani zifukwa zake.

## Matanthauzo a mawu

**Chiganizo**: Gulu la mawu lokhala ndi mneni ndipo limapereka ganizo lomveka bwino.

## Mabuku


Banda, FK, (2003). *Methods of teaching Chichewa.* Domasi: Domasi College of Education.

Nankwenya, IAJ, (1992). *Zofunika mu galamala ya Chichewa*. Blantyre: Dzuka.

Nkhoma, W, (2016). *Kuphunzira Chichewa: malamulo a chiyankhulo*. Zomba: Chanco Publications.


## Kuwerenga koonjezera


Chauma, AM and Ngoma, SJL, (2014). *Tizame m'Chichewa* (3rd ed.). Blantyre: Bookland International.

Nkhoma, WA, (1999). *Kuphunzira Chinyanja*. Zomba: Chanco Publications.

## MUTU 8 Kuphunzitsa nthambi za chiganizo

| | |
|---|---|
| **Luso** | Kugwiritsa ntchito malamulo achiyankhulo |
| **Nthawi** | Maola 3 |
| **Chigawo** | Chachitatu |

### Chiyambi

M'mbuyomu, mudaphunzitsapo malamulo achiyankhulo pa mitu yosiyanasiyana. Mwachitsanzo, m'mutu 7, mudaphunzira tanthauzo la chiganizo ndi mitundu yake yomwe ndi chiganizo chopanda nthambi, chiganizo cha ziganizo zingapo, chiganizo chanthambi ndi chiganizo cha ziganizo zanthambi.

M'mutu uno, muphunzira za nthambi za chiganizo ndi mitundu yake.

### Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- asiyanitsa nthambi za chiganizo.
- afotokoza ntchito za mitundu yosiyanasiyana ya nthambi ya chiganizo yosaima payokha.
- aphunzitsa nthambi za chiganizo.

### Mawu otsogolera

Nthambi ya chiganizo ndi gulu la mawu m'chiganizo lomwe limakhala ndi mneni wakewake.

Pali mitundu iwiri ya nthambi za chiganizo: nthambi yoima payokha ndi nthambi yosaima payokha. Palinso mitundu itatu ya nthambi ya chiganizo yosaima payokha: nthambi yosaima payokha yadzina, nthambi yosaima payokha yamfotokozi ndi nthambi yosaima payokha yamuonjezi.

Nthambi yosaima payokha yamuonjezi ilinso ndi mitundu yakeyake iyi: yamchitidwe, yamalo, yanthawi, yachifukwa, yacholinga, yolabadira ndi yapokhapokha.

Kudziwa nthambi za chiganizo kumathandiza ophunzira kugwiritsa ntchito chiyankhulo moyenera makamaka pamene akupanga ziganizo. Aphunzitsi muyenera kudziwa kaphunzitsidwe koyenera kuti ophunzira amvetse za ziganizo zanthambi.

### Ntchito 1 Kusiyanitsa nthambi za ziganizo

Ziganizo zimakhala zosiyanasiyana. Ziganizo zina zimakhala ndi nthambi zosiyanasiyanso. N'kofunika kuzindikira kusiyana kwa nthambizi kuti muzikaphunzitsa mosavuta. Tsopano musiyanitsa nthambi za ziganizo. Kenaka, mupanga ziganizo zanu zokhala ndi nthambi.

**Zochita 1 Kupeza nthambi za ziganizo zosaima pazokha**

1 Pezani zitsanzo za nthambi za ziganizo zosaima pazokha kuchokera m'mabuku a ophunzira a Sitandade 7 ndi 8.
2 Kambiranani kusiyana pakati pa nthambi ya chiganizo yoima

payokha ndi nthambi yosaima payokha.
3 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kupanga ziganizo za nthambi**

1 Pangani ziganizo zokhala ndi nthambi.
2 Siyanitsani nthambizo posankha zosaima pazokha.
3 Zukutani ziganizo zomwe anzanu apanga.

## Ntchito 2 Kufotokoza ntchito za nthambi za ziganizo zosaima pazokha

Nthambi za chiganizo zosaima pazokha zimagwira ntchito zosiyanasiyana molingana ndi mtundu wake. Tsopano mufotokoza ntchito za nthambi yosaima payokha yadzina, yamfotokozi ndi yamuonjezi.

**Zochita 1 Kukambirana ntchito za nthambi za ziganizo zosaima pazokha**

1 Pezani nthambi zosaima pazokha za mitundu yosiyanasiyana kuchokera m'mabuku a ophunzira m'sukulu a Sitandade 7 ndi 8.
2 Kambiranani ntchito za nthambi za ziganizo zomwe mwapeza.
3 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kuzindikira nthambi ya chiganizo yadzina**

1 Pezani nthambi yachiganizo yadzina m'ziganizo zomwe mwapatsidwa.
2 Kambiranani momwe mungazindikirire nthambi yosaima payokha yadzina.
3 Pangani ziganizo zokhala ndi nthambi yadzina.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 3 Kuzindikira nthambi ya chiganizo yamfotokozi**

1 Kambiranani momwe mungadziwire nthambi ya chiganizo yosaima payokha yamfotokozi.
2 Pangani ziganizo zokhala ndi nthambizi.
3 Sonyezani anzanu zomwe mwalemba.

**Zochita 4 Kuzindikira nthambi ya chiganizo yamuonjezi**

1 Kambiranani ntchito zosiyanasiyana za muonjezi.
2 Pangani ziganizo zokhala ndi nthambi zosaima pazokha za muonjezi.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

## Ntchito 3 Kuphunzitsa nthambi za chiganizo

Tsopano muonerera aphunzitsi anu pamene akuphunzitsa. Kenaka, muphunzitsa mtundu wa nthambi za chiganizo womwe mwapatsidwa.

**Zochita 1 Kuonerera phunziro la nthambi za chiganizo**

1 Kambiranani momwe mungaphunzitsire mtundu wanthambi za chiganizo womwe mwapatsidwa.

2 Onererani pamene aphunzitsi anu akuphunzitsa nthambi za chiganizo.
3 Perekani maganizo anu pa momwe phunzirolo layendera.

**Zochita 2 Kuphunzitsa nthambi za chiganizo**

1 Konzekerani kuphunzitsa mtundu wa nthambi za chiganizo womwe mwapatsidwa.
2 Phunzitsani mtundu wa nthambi ya chiganizoyo potsatira njira yomwe mwasankha.
3 Unikani momwe maphunziro ayendera.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mukhale ndi mabuku okwanira a ophunzira a Sitandade 7 ndi 8.
- Mupezeretu zitsanzo za nthambi za chiganizo zoima pazokha ndi zosaima pazokha za dzina, mfotokozi ndi muonjezi.
- Muonetsetse kuti ophunzira akufotokoza bwino ntchito za nthambi zosiyanasiyana za ziganizo pophunzitsa.
- Mukonzekere kuphunzitsa nthambi za ziganizo.
- Muombe mkota pa zomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira tanthauzo ndi mitundu ya nthambi za chiganizo. Mwafotokoza ntchito za nthambi za chiganizo mogwirizana ndi mitundu yawo. Pomaliza, mwasonyeza momwe mungaphunzitsire nthambi za chiganizo.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Kodi pali kusiyana kotani pakati pa nthambi yoima payokha ndi nthambi yosaima payokha ya chiganizo?
2 Mungamuthandize bwanji wophunzira kusiyanitsa nthambi ya muonjezi yacholinga ndi nthambi ya muonjezi yachifukwa.
3 Fotokozani momwe mungaphunzitsire phunziro la 'nthambi za chiganizo' ndipo mutchule njira yophunzitsira yomwe mwasankha.

## Matanthauzo a mawu

**Nthambi ya chiganizo**: gulu la mawu m'chiganizo lomwe limakhala ndi mneni wakewake.

**Nthambi yoima payokha**: gulu la mawu lokhala ndi mwininkhani komanso mneni ndipo limapereka ganizo lomveka bwino.

**Nthambi yosaima payokha**: gulu la mawu lokhala ndi mneni wakewake koma silimapereka ganizo lomveka bwino palokha.

## Mabuku

Banda, FK, (2003). *Methods of teaching Chichewa*. Domasi: Domasi College of Education.
Nankwenya, IAJ, (1992). *Zofunika mu galamala ya Chichewa*. Blantyre: Dzuka Publishing Company Limited.
Nkhoma, W, (2016). *Kuphunzira Chichewa: malamulo a chiyankhulo*. Zomba: Chanco Publications.

## Kuwerenga koonjezera

Chauma, AM & Ngoma, SJL, (2014). *Tizame m'Chichewa* (3rd ed.).

Nkhoma, WA, (1999). *Kuphunzira Chinyanja*. Zomba: Chanco Publications

MUTU 9

# Kuphunzitsa ndi kuyesa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani/nthano, macheza ndi sewero

| | |
|---|---|
| **Luso** | Kuganiza mozama |
| **Nthawi** | Maola 3 |
| **Chigawo** | Chachitatu |

## Chiyambi

M'mbuyomu, mudaphunzira momwe mungaphunzitsire ophunzira a m'sukulu za pulayimale luso la kuzukuta ndakatulo/nyimbo, sewero ndi nthano. Mudaphunziranso mfundo zomwe muyenera kutsatira pozukuta mituyi monga kupeza atengambali, malo ndi nthawi yochitikira nkhani/nthano ndi tsatanetsatane wa zochitika komanso mfundo yaikulu.

M'mutu uno, muphunzira momwe mungaphunzitsire ndi kuyesa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani/nthano, macheza ndi sewero. Muunika momwe munkaphunzitsira kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano ndi sewero m'sukulu zomwe munkaphunzitsa. Pomaliza, mufufuza njira zothetsera mavuto omwe munkakumana nawo komanso musonyeza momwe mungaphunzitsire mituyi moyenera.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- aphunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani/nthano, macheza ndi sewero.

## Mawu otsogolera

Kuzukuta ndi luso lopambana kwambiri pa moyo wa munthu wina aliyense. Pa lusoli, timaunika ndakatulo, nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani, nthano, macheza, sewero ndi zina mwakuya kuti timvetse bwino tanthauzo la zomwe zikukambidwa. Motero, n'koyenera kukhala ndi lusoli kuti timvetse bwino zomwe ena akufotokoza, zomwe tikuwerenga komanso kuti tiyankhule zogwira mtima kwa anthu ena.

Aphunzitsi muyenera kudziwa bwino mfundo zoyenera kutsatira pozukuta ndakatulo/nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani/nthano, macheza ndi sewero kuti muthandize ophunzira moyenera.

Pophunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani/nthano, macheza ndi sewero unikirani ophunzira mfundo izi:

- Ndani akuyankhula m'ndakatulo kapena nyimbo/akutenga mbali m'nkhani/nthano ndi sewero?
- Akuti chiyani/akutenga mbali yanji?
- Akuyankhula ndi yani/akuchita chiyani?
- N'chifukwa chiyani akuyankhula/akuchita zimenezo?
- Kodi woyankhulayo kapena mtengambaliyo ndi wosangalala, wachisoni, wokhumudwa, wodabwa?

- Kodi ndi mfundo yaikulu iti yomwe ili mu ndakatulo/nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani/nthano, macheza ndi sewero?
- Kodi zipangizo za nsetso (mawu apadera monga mpeputso, msemphano, voko ndi chiyerekezo) zagwiritsidwa ntchito bwanji?

**Ntchito Kuphunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, zilapi/ndagi, nkhani/nthano, macheza ndi sewero**

Mu ntchito ino, muunika momwe munkaphunzitsira kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano ndi sewero m'sukulu zomwe munkaphunzitsa. Pomaliza, muphunzitsa ntchitozi.

**Zochita 1 Kufotokoza momwe munkaphunzitsira kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero**

1 Fotokozani momwe munkaphunzitsira kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano ndi sewero m'sukulu zomwe munkaphunzitsa.
2 Kambiranani mavuto omwe munkakumana nawo pophunzitsa maphunzirowo.
3 Perekani njira zomwe mungagwiritse ntchito kuti muthetse mavuto omwe munkakumana nawo.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero**




1 Kambiranani mfundo zoyenera kutsatira pozukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero.
2 Fufuzani ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero kuchokera m'mabuku a ophunzira.
3 Zukutani ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero zomwe mwapeza pogwiritsa ntchito mfundo zomwe mwakambirana.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 3 Kusonyeza kuphunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero**

1 Unikani ndondomeko yomwe munkagwiritsa ntchito pophunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano,

macheza ndi sewero m'sukulu zomwe munkaphunzitsa.

2 Kambiranani momwe mungaphunzitsire kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero pogwiritsa ntchito njira zomwe mwakambirana mu ntchito 1.
3 Sonyezani kuphunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero pogwiritsa ntchito njirazo.
4 Zukutani phunziro lomwe mwaonera.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Limbikitsani ophunzira kupereka njira zothetsera mavuto omwe ankakumana nawo.
- Mukhale ndi mabuku okwanira.
- Mukonzeretu mfundo zoyenera kutsatira pozukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano ndi sewero.
- Muombe mkota pa ntchito yomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaunika momwe munkaphunzitsira kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero. Mwazukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero komanso mwaphunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero pogwiritsa ntchito njira zoyenera.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Fotokozani kufunika kophunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero m'sukulu zapulayimale.
2 Kodi ndi mfundo ziti zomwe zingakuthandizeni kuphunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero moyenera?
3 Perekani ndondomeko yomwe mungatsatire pophunzitsa kuzukuta ndakatulo/nyimbo, nkhani/nthano, macheza ndi sewero.

## Matanthauzo a mawu

**Mpeputso:** mawu osaumitsa thupi omwe amalowa m'malo mwa oipa.

**Msemphano:** mawu onena zina koma akutathauza zina.

**Voko:** kukuza zinthu zazing'ono/mawu omwe amanena moonjezera kapena kusinjirira chabe.

**Chiyerekezo:** kufananitsa mopanda chindunji zinthu ziwiri zosiyana.

**M'malere:** kathedwe ka nkhani komuchititsa womvera kapena wowerenga kufunabe kudziwa zambiri.

## Mabuku

Abrams, MH & Harpham, GG, (2005). *A glossary of literary terms (9th ed.).* Boston: Cengage Learning.

Moto, F, (2001). *Trends in Malawian literature.* Zomba: Chancellor College Publications.

Nkhoma, W, (2016). *Guide to literary terms with Chichewa equivalents and examples.* Zomba: Chanco.

## Kuwerenga koonjezera

Mjaya, ANU, (2001). *Introduction to literary criticism: lingistics and African languages module 4*. Domasi: Domasi College of Education.

Ngoma, SJL & Nkhoma, W, (2014). *Nsinjiro za chiyankhulo ndi maziko a nkhani za mchezo, ndakatulo ndi zisudzo*. Blantyre: Bookland.

Sitima, JG, (2001). *Mtondo: kufotokozera za ndakatulo, zifanifani, nyimbo ndi ndagi*. Zomba: Chanco Publications.

# MUTU 10 Kuphunzitsa nsinjiro zachiyankhulo

| | |
|---|---|
| **Luso:** | Kuganiza mozama |
| **Nthawi** | Maola 5 |
| **Chigawo** | Chachitatu |

## Chiyambi

Kukulitsa luso la kuganiza mozama kumachitika pophunzitsa ntchito zosiyanasiyana monga zilapi, nthano ndi sewero. Palinso ntchito zina zomwe zimathandiza kukulitsa luso la kuganiza mozama. Ntchitozi ndi nsinjiro zachiyankhulo monga ntchedzero/zifanifani, zining'a, nseketso, mipeputso ndi mikuluwiko. Ntchitozi zimakometsanso chiyankhulo. Choncho n'kofunika kuti ophunzira azitha kuzigwiritsa ntchito moyenera.

M'mutu uno, muphunzira momwe mungaphunzitsire ntchito zina zokhudza ntchedzero/zifanifani, zining'a, nseketso, mpeputso ndi mikuluwiko. Izi zikuthandizani kuti muziphunzitsa luso la kuganiza mozama pochita ntchito zosiyanasiyana zokhudza nsinjiro za chiyankhulo.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:

- afotokoza mitundu ya nsinjiro zachiyankhulo.
- asintha nsinjiro zachiyankhulo zosiyanasiyana kukhala m'mitundu ina.
- asonyeza kaphuzitsidwe ka nsinjiro zachiyankhulo.

## Mawu otsogolera

Nsinjiro za chiyankhulo ndi mawu omwe amagwiritsidwa ntchito poyankhula kapena polemba ndi cholinga chofuna kukometsera chiyankhulo. Pali mitundu yosiyanasiyana ya nsinjiro za chiyankhulo. Ina mwa mitunduyi ndi zining'a, ntchedzero/zifanifani, mipeputso, nseketso, mikuluwiko ndi miyambi. Nsinjiro za chiyankhulo zimagwira ntchito zosiyanasiyana. Mwachitsanzo, zimakometsa chiyankhulo komanso zimathandiza kuyankhula kapena kulemba nkhani mophiphiritsa n'cholinga choti ena asadziwe zomwe munthu akutanthauza. Nsinjiro zachiyankhulo zimathatndizanso kukulitsa luso la kuganiza mozama.

Kuti muphunzitse bwino phunziro la nsinjiro za chiyankhulo, muyenera kudziwa mitundu yosiyanasiyana ya nsinjirozo. Muyeneranso kudziwa bwino zitsanzo za mitundu yosiyanasiyanayo ndi ndondomeko yoyenera kutsatira pophunzitsa.

### Ntchito 1 Kufotokoza mitundu yosiyanasiyana ya nsinjiro zachiyankhulo

Muli kusekondale, mudaphunzira za nsinjiro zachiyankhulo zosiyanasiyana. M'gawo lino, muunika mitundu ya nsinjiro zachiyankhulozi. Kenaka, mupeza

mikuluwiko yofanana komanso yotsutsana m'matanthauzo.




**Zochita 1 Kukambirana mitundu ya nsinjiro za chiyankhulo**

1 Kambiranani matanthauzo ndi zitsanzo za nsinjiro za chiyankhulo izi:
   a. zining'a
   b. ntchedzero/zifanifani
   c. mipeputso
   d. nseketso
   e. mikuluwiko
   f. miyambi
2 Fufuzani nsinjiro za chiyankhulozi m'mabuku a ophunzira.
3 Kambiranani matanthauzo a nsinjiro zomwe mwapeza.
4 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kukambirana mikuluwiko yofanana m'matanthauzo**

1 Kambiranani kusiyana kwa mkuluwiko ndi mwambi.
2 Fufuzani mikuluwiko yosiyanasiyana m'mabuku a ophunzira.
3 Kambiranani matanthauzo a mikuluwiko yomwe mwapeza.
4 Pezani mikuluwiko yofanana m'matanthauzo.
5 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Zochita 3 Kukambirana mikuluwiko yotsutsana m'matanthauzo**

1 Fufuzani mikuluwiko yosiyanasiyana m'mabuku a ophunzira.
2 Kambiranani matanthauzo a mikuluwiko yomwe mwapeza.
3 Pezani mikuluwiko yotsutsana m'matanthauzo.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Ntchito 2 Kusintha nsinjiro zachiyankhulo kukhala m'mitundu ina**

Mu ntchito 1, munakambirana mitundu yosiyanasiyana ya nsinjiro za chiyankhulo. Tsopano mukambirana momwe mungasinthire ntchedzero/zifanifani kukhala zining'a, zining'a kukhala ntchedzero/zifanifani komanso mikuluwiko kukhala ntchedzero/zifanifani.

**Zochita 1 Kusintha ntchedzero/zifanifani kukhala zining'a**

1 Kambiranani matanthauzo a ntchedzero/zifanifani.
2 Pezani ntchedzero/zifanifani m'mabuku a ophunzira.
3 Kambiranani kusiyana kwa ntchedzero ndi zining'a.
4 Kambiranani momwe mungasinthire ntchedzero/zifanifani kukhala zining'a.
5 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kusintha zining'a kukhala ntchedzero/zifanifani**

1 Kambiranani momwe ntchedzero/zifanifani zimapangidwira.
2 Pezani zining'a m'mabuku a ophunzira.
3 Sinthani zining'azo kukhala ntchedzero/zifanifani.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 3 Kusintha mikuluwiko kukhala ntchedzero/zifanifani**

1 Pezani mikuluwiko m'mabuku a ophunzira.
2 Sinthani mikuluwikoyo kukhala ntchedzero/zifanifani.
3 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

## Ntchito 3 Kuphunzitsa nsinjiro za chiyankhulo

M'gawo lino, mukambirana za mipeputso ndi nseketso. Kenaka, musonyeza momwe mungaphunzitsire nsinjiro zachiyankhulo.

**Zochita 1 Kupereka matanthauzo a mipeputso**

1 Kambiranani tanthauzo la mpeputso.
2 Fufuzani zitsanzo za mpeputso.
3 Fotokozani kufunika kogwiritsira ntchito mipeputso.
4 Fotokozani matanthauzo a mipeputso yomwe mwapeza.
5 Fotokozerani anzanu zomwe mwapeza.

**Zochita 2 Kupereka matanthauzo osiyana a nseketso**

1 Kambiranani tanthauzo la nseketso.
2 Fufuzani zitsanzo za nseketso m'mabuku a ophunzira.
3 Kambiranani matanthauzo awiri osiyana a nseketso iliyonse.
4 Fotokozerani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 3 Kuphunzitsa nsinjiro za chiyankhulo**

1 Konzekerani phunziro la nsinjiro za chiyankhulo lomwe mwapatsidwa.
2 Kambiranani momwe mungaphunzitsire phunzirolo.
3 Sonyezani momwe mungaphunzitsire phunziroli.
4 Zukutani maphunzirowo.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mupezeretu zitsanzo zoyenera za nsinjiro za chiyankhulo izi: zining'a, ntchedzero/zifanifani, mipeputso, nseketso ndi mikuluwiko.
- Mupezeretu mabuku a ophunzira omwe muli nsinjiro za chiyankhulo zosiyanasiyana.
- Muonetsetse kuti ophunzira akuphunzitsa potsatira ndondomeko yoyenera.
- Muombe mkota pa zomwe ophunzira achita.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Siyanitsani mitundu ya nsinjiro za chiyankhulo zotsatirazi:
   a. chining'a ndi chifanifani
   b. mkuluwiko ndi mwambi
   c. chining'a ndi mpeputso
   d. chining'a ndi mkuluwiko

2 Perekani matanthauzo awiri osiyana a nseketso zotsatirazi:
   a. Nkhuku ndatengayi njomanga.
   b. Kodi kholowa m'kabudula angamere?
   c. Achimwene, kodi m'kamwa mumanunkha?
   d. Lero tigonera mbatata.
   e. Kodi ufa ukadya?

3 Fotokozani kufunika kophunzitsa nsinjiro za chiyankhulo m'sukulu zapulayimale.

## Kufotoza mwachidule

M'mutu uno, mwaphunzira mitundu ya nsinjiro za chiyankhulo izi: zining'a, ntchedzero/zifanifani, mipeputso, nseketso, mikuluwiko ndi miyambi. Mwakambirana kasinthidwe ka nsinjiro za chiyankhulo kupita ku mitundu ina. Mwaphunziranso momwe mungaphunzitsire nsinjirozi pokulitsa luso la kuganiza mozama mwa ophunzira. Pomaliza, mwasonyeza kuphunzitsa nsinjiro za chiyankhulo.

## Matanthauzo a mawu

**Chining'a**: Mawu amodzi kapena gulu lochepa la mawu lomwe limakhala ndi tanthauzo lobisika.

**Ntchedzero/chifanifani**: Mawu omwe matanthauzo ake ndi osereula omwe amaseketsa kapena kukwiyitsa munthu wosereula naye.

**Mpeputso**: Mawu osaumitsa thupi omwe amalowa m'malo mwa oipa monga otukwana ndi ochititsa mantha.

**Nseketso**: Chiganizo chokhala ndi matanthauzo ambiri.

**Mkuluwiko**: Mutu wa mwambi ndipo umakhala ndi phunziro.

## Mabuku

Malawi Institute of Education, (2008). *Maphunziro a m'sukulu zauphunzitsi m'Malawi*: *buku la mphunzitsi*. Domasi: MIE.

Malawi Institute of Education, (2008). *Chichewa buku la ophunzira la Sitandade 7*. Domasi: MIE.

# MUTU 11 Kuphunzitsa mtantho wa mawu

**Luso** Kuganiza mozama
**Nthawi** Maola 2
**Chigawo** Chachitatu

## Chiyambi

M'mbuyomu, mudaphunzira ntchito zosiyanasiyana zomwe mungaphunzitse ophunzira a kupulayimale kuti akhale ndi luso la kuganiza mozama. Zina mwa ntchitozi ndi monga kufotokoza ndi kupeza phunziro m'miyambi, kupereka matanthauzo a mikuluwiko komanso zining'a. Mudaphunziranso kuti ntchitozi zimathandiza kulimbikitsa chikhalidwe cha makolo.

M'mutu uno, muphunzira momwe mungaphunzitsire mtantho wa mawu. Mufotokoza tanthauzo la mtantho wa mawu, kufunika kophunzitsa mtantho wa mawu komanso momwe mungaphunzitsire.

## Zizindikiro za kakhozedwe

Pakutha pa mutu uno, ophunzira:


- afotokoza kufunika kophunzitsa mtantho wa mawu.
- asonyeza kuphunzitsa mtantho wa mawu.

## Mawu otsogolera

Mtantho wa mawu ndi sewero lolemba mawu mopingasa ndi motsitsa. Mtantho wa mawu ndi wofunika pophunzitsa chiyankhulo chifukwa umathandiza ophunzira kuganiza mozama, kudziwa kalembedwe ka mawu komanso ndi njira yosangalatsa yophunzitsira mawu.

**Chitsanzo cha mtantho wa mawu**:

Lembani mopingasa kapena motsitsa malembo opanga mawu omwe ndi matanthauzo a ziganizo zili m'musimo.  Malembo opanga mawu alionse aziyambira pomwe pali nambala. (Ntchitoyi yachokera m'buku la ophunzira, Chichewa Sitandade 5; tsamba 92).




**Mopingasa**

1 nthenda yotsokomoletsa
3 fika kumalo ambiri
5 mtundu wa nthenda yotulutsa timatuza pathupi
6 nthenda yosachizika
8 samalira munthu wodwala
9 tulutsa mawu ndi misozi chifukwa cha ululu

**Motsitsa**

1 nthenda yotenthetsa thupi ndi yofiiritsa maso yomwe ana amadwala kawirikawiri
2 nthenda yomwe imatulutsa manthongo m'maso
4 gwero la kudwala kapena kusamva bwino m'thupi
7 nthenda yotulutsa matuza pathupi omwe amatuluka mafinya
8 khala osapeza bwino m'thupi chifukwa cha matenda

**Mayankho**
**Mopingasa**

1 Chifuwa
3 Fala
5 Katsabola
6 Edzi
8 Dwazika
9 Lira

**Motsitsa**

1 Chikuku
2 Maso
4 Nthenda
7 Mphere
8 Dwala

Pomaliza, muyenera kumvetsetsa ndondomeko yomwe mungatsatire pophunzitsa mtantho wa mawu kuti ntchitoyi ikhale yopindulira ophunzira. Mutu uno wapereka tsatanetsatane wa momwe mungaphunzitsire mtantho wa mawu.

### Ntchito 1 Kufotokoza kufunika kophunzitsa mtantho wa mawu

Monga sewero, mtantho wa mawu ndi njira yophunzirira yosangalatsa. M'gawo lino, mufotokoza kufunika kophunzitsa mtantho wa mawu.

**Zochita 1 Kufotokoza momwe munkaphunzitsira mtantho wa mawu**

1 Fufuzani zitsanzo za mtantho wa mawu m'mabuku a ophunzira.
2 Kambiranani tanthauzo la mtantho wa mawu.
3 Fotokozani momwe munkaphunzitsira mtantho wa mawu m'sukulu zomwe munkaphunzitsa.
4 Kambiranani mavuto omwe mudakumana nawo pophunzitsa mtantho wa mawu.
5 Perekani njira zomwe mungagwiritse ntchito kuti muthetse mavuto omwe munkakumana nawo.

**Zochita 2 Kufotokoza kufunika kwa mtantho wa mawu**

1 Kambiranani kufunika kophunzitsa mtantho wa mawu.
2 Fotokozani mfundo zoyenera kutsatira pophunzitsa mtantho wa mawu.
3 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

### Ntchito 2 Kuphunzitsa mtantho wa mawu

Mwakambirana kuti mtantho wa mawu ndi wofunika kwambiri pophunzitsa chiyankhulo. M'gawo lino, mufotokoza ndondomeko yoyenera kutsatira pophunzitsa mtantho wa mawu. Pomaliza, musonyeza momwe mungaphunzitsire mtantho wa mawu kwa ophunzira akupulayimale.

**Zochita 1 Kukambirana ndondomeko yophunzitsira mtantho wa mawu**

1 Unikani ndondomeko yomwe munkatsatira pophunzitsa mtantho wa mawu.
2 Fotokozani mavuto omwe mudakumana nawo pogwiritsa ntchito ndondomeko yomwe mwatchula.
3 Kambiranani ndondomeko yoyenera yophunzitsira mtantho wa mawu.
4 Uzani anzanu zomwe mwakambirana.

**Zochita 2 Kuonerera phunziro la mtantho wa mawu**

1 Kambiranani momwe mungaphunzitsire mtantho wa mawu.
2 Onererani pamene aphunzitsi anu akuphunzitsa mtantho wa mawu.
3 Perekani maganizo anu pa momwe phunzirolo layendera.

**Zochita 3 Kuphunzitsa mtantho wa mawu**

1 Konzani ndondomeko yophunzitsira mthantho wa mawu mu kalasi lomwe mwasankha.
2 Phunzitsani mtantho wa mawu pogwiritsa ntchito ndondomeko yomwe mwakonza.
3 Zukutani maphunzirowo.

**Malangizo kwa mphunzitsi**

- Mukonzeretu ndondomeko yophunzitsira mtantho wa mawu.
- Mupezeretu mtantho wa mawu woti muphunzitsire.
- Muombe mkota pa ntchito zomwe ophunzira achita.

## Kufotokoza mwachidule

M'mutu uno, mwaunika momwe munkaphunzitsira mtantho wa mawu komanso mwafotokoza tanthauzo ndi kufunika kwake. Mwaunikanso ndondomeko yoyenera kugwiritsa ntchito pophunzitsa mtantho wa mawu, mfundo zoyenera kuganizira pophunzitsa ndi momwe mungaphunzitsire. Pomaliza, mwasonyeza kaphunzitsidwe koyenera ka mtantho wa mawu.

## Kudziunika ndi kudziyesa

1 Mwapeza kuti aphunzitsi ena pa sukulu yanu saphunzitsa mtantho wa mawu m'makalasi awo. Kodi mungapereke malangizo otani kwa aphunzitsi otere?

2 Fotokozani ndondomeko yoyenera yophunzitsira mtantho wa mawu.

3 Ndi mfundo ziti zomwe mungatsate kuti phunziro la mtantho wa mawu m'kalasi lanu likhale losangalatsa ndi lopatsa chidwi kwa ophunzira?

4 Lembani chitsanzo cha mtantho wa mawu wophunzitsira malamulo a chiyankhulo kapena zilapi kwa ophunzira a Sitandade 5.

## Matanthauzo a mawu

**Mtantho wa mawu**: Sewero lolemba mawu mopingasa ndi motsitsa

## Mabuku


Chilora, H G & Kathewera, REM, (2014). *Chichewa buku la ophunzira a Fomu 2*. Blantyre: Dzuka publishing company limited.

Malawi institute of Education, (2008). *Maphunziro a m'sukulu zapulayimale m'Malawi: Chichewa buku la mphunzitsi la Sitandade 7*. Domasi: Malawi Institute of Education.


## Kuwerenga koonjezera


Chauma, AM & Ngoma, SJL, (2014). *Tizame m'Chichewa* (3rded.). Blantyre: Bookland International.